## PHUNZIRO LA 39

1. Kodi mtsogoleri watsopano wa a Isirayeli amene Mulungu anamusankha kuti aloŵe m'malo mwa Mose anali ndani?
-Yoswa.

2. Kodi Mulungu anasunga lonjezo lache ndikulipereka dziko la Kanani kwa zidzukulu za Aburahamu?
-Inde.

3. Kodi a Isirayeli anachita chiyani Yoswa atamwalira?
-Yoswa atamwalira, a Isirayeli anamukana Mulungu ndipo anali oyipitsitsa.
-Yoswa atamwalira, a Isirayeli anapanga mafano ndikumaŵapembedza mafanowo m'malo mwa Mulungu.

4. Kodi ndani amene anaŵanamiza a Isirayeli kuti amukane Mulungu ndikumaŵapembedza mafano a Baala ndi Ashiloti?
-Satana.

5. Ngati tikumpembedza wina wake kapena china chake osakhala Mulungu, kodi tikumupembedza ndani?
-Satana.

6. Kodi chifukwa chiyani Satana amafuna kuti anthu adzipembedza mafano?
-Chifukwa chakuti Satana amamuda Mulungu, chomcho safuna kuti wina aliyense adzimupembedza Mulungu.
-Chifukwa chakuti Satana amaŵada anthu onse ndipo samafuna kuti Mulungu aŵapulumutse anthuwo.

7. Kodi Mulungu anaŵapatsa chilango chotani a Isirayeli chifukwa chopembedza mafano?

-Mulungu anatumiza adani a a Isirayeli kuti akaŵawonongere a Isirayeli mbewu zawo zonse.
-Mulungu anaŵatumiza adani a a Isirayeli kuti akabere a Isirayeli ziweto zawo zonse.
-Mulungu anaŵatumiza adani a a Isirayeli kuti akaŵapange a Isirayeli onse kukhala akapolo.

8. A Isirayeli atavomereza kuchimwa kwawo, ndikumupempha Mulungu kuti aŵapulumutse, kodi Mulungu anachita chiyani?
-A Isirayeli ataŵavomereza machimo awo, ndikumupempha Mulungu kuti aŵapulumutse, Mulungu anasankha amuna ndi akazi mwa a Isirayeliwo kuti aŵatsogolere iwowo poŵagonjetsa adani awo.

9. Kodi amuna ndi akazi amene anasankhidwa ndi Mulungu kuti aŵatsogolere a Isirayeli kuti aŵagonjetse adani awowo, ankatchedwa kuti ndani?
-Oweruza.

10. Kodi chifukwa chiyani Mulungu ankaŵakondabe ndipo kuŵateteza a Isirayeli?
-Chifukwa chakuti Mulungu anapereka lonjezo kwa Aburahamu, Isaki ndi Yakobo kuti adzakhala ndi zidzukuru zambiri ndipo udzakhala mtundu wawukuru kwambiri.
-Chifukwa chakuti Mulungu anapereka lonjezo lakuti adzatumiza Mpulumutsi kudzera mu zidzukulu za a Isirayeli.
-Chifukwa chakuti Mulungu analonjeza kuti adzatumiza uthenga wache , Bayibulo, kupitira mu zidzukuru za a Isirayeli.

11. Kodi Oweruza omaliza wa a Isirayeli amene Mulungu anamusankha anali ndani?
-Samuyele.



-Mulungu ankanena kuti adikira kaye osapereka msanga chilango cha machimo kwa chaka china chimodzi mpaka malipiro abwino a machimowo atachitika.

-Kodi magazi a nyama ankatha kulipira pa sambi za a Isirayeli?
-Iyayi.

-Kodi chifukwa chiyani magazi a nyama sanakatha kulipira pa sambi za anthu?

-Chifukwa chakuti sambi ziyenera kulipiridwa ndi imfa ya munthu wochimwa.

-Solomoni atamwalira, a Isirayeli sanagwirizane pa za munthu amene angaloŵe m'malo mwache.

-Chomcho, mitundu 12 ya a Isirayeli inagaŵikana ndikukhala mitundu iŵiri.

-Mitundu 10 ya ku mpoto, inakhala mtundu umodzi.

-Mitundu yiŵiri ya kumwera, inakhala mtundu umodzi.

-Mitundu 10 ya ku mpoto ija inkatchedwa kuti a Isirayeli.

-Mitundu iŵiri ya kumwera ija inkatchedwa kuti Ayuda.

-Mafumu ambiri anaŵalamulira a Isirayeli, ndipo mafumu ambirinso anaŵalamulira Ayuda.

-Ambiri mwa mafumuwo sankakhulupilira mwa Mulungu.

-Apang'ono okha mwa mafumuwo ndi amene ankakhulupilira mwa Mulungu.

mumangira Mulungu mchipululu muja.

-Sakasa la Mulungu linali ndi chipinda choyamba chimene chinkatchedwa kuti Chipinda  Chopatulika.

-Nyumba ya Mulungu nayonso inali ndi chipinda choyamba chimene chinkatchedwa kuti Chipinda Chopatulika.

-Sakasa la Mulungu linali ndi chipinda chachiŵiri chimene chinkatchedwa kuti Chipinda Chopatulikitsitsa.

-Nyumba ya Mulungu nayonso inali ndi chipinda chachiŵiri chimene chinkatchedwa kuti Chipinda Chopatulikitsitsa.

-Sakasa la Mulungu linali ndi nsaru yotchinga pakati pa zipinda ziŵiri zija.

-Nyumba ya Mulungu nayonso inali ndi nsaru yotchinga pakati pa zipinda ziŵiri zija.

-Chifukwa chakuti Mulungu ndi oyera ndipo amadana ndi tchimo lina lililonse, wamsembe wamkulu ndi amene amaloredwa kuloŵa M'chipinda Chopatulikitsitsacho kamodzi pa chaka.

-Chifukwa chakuti Mulungu ndi oyera ndipo amadana ndi tchimo lina lililonse, wamsembe wamkulu ankayenera kutenga magazi a nyama ndikuloŵa nawo M'chipinda Chopatulikitsitsa chija ndi kuŵamwaza pamwamba pa Likasa la Chipangano.

-Kodi Mulungu ankayenera kuti achite chiyani akaŵawona magazi a nyama amene wamkulu wamsembe amawawaza pa Likasa la Chilanga lija?



12. Kodi a Isirayeli anamupempha kuti achite chiyani Samuyele asanamwalire?
-A Isirayeli anamupempha Samuyele kuti aŵasankhire mfumu kuti adziŵatsogolera.

13. Kodi chifukwa chiyani Samuyele anakwiya ndi zimenezi?
-Samuyele anakwiya ndi zimenezi chifukwa chakuti a Isirayeli ankamukana Mulungu kuti akhale Mfumu yawo.

-Mulungu anamusankha Sawulo kuti akhale mfumu yoyamba ya a Isirayeli.

-Chifukwa chakuti Mulungu ndi amene anamusankha Sawulo, Mulunguyo ankafuna kuti Sawulo adzimumvera Iye.

-Koma Sawulo sankamumvera Mulungu.

-Chomcho Samuyele anamuwuza Sawulo kuti Mulungu wasankha mamuna wina kuti akhale mfumu wa a Isirayeli.

Tiyeni tiŵerenge 1 Samuyele 13:13-14

13-Samuyele anati kwa Sawulo, "Wapanga zinthu zopusa kwambiri. Siwunasunge lamulo limene Ambuye, Mulungu wako anakupatsa; unakakhala kuti wasunga, anakawukhazikitsa ufumu wako pa Isirayeli mpaka kalekale.
14-Koma tsopano ufumu wako siwupitilira; Ambuye afuna mamuna amene akumufuna ndipo amusankha iye kukhala mtsogoleri wa anthu ache, chifukwa chakuti siwunasunge lamulo la Ambuye."

-Pamene Sawulo sanamumvere Mulungu, kodi Mulungu anamusankha ndani kuti akhale mfumu ya a Isirayeli yotsatira?
-Davide.

-Mulungu anamusankha Davide kukhala mfumu yachiŵiri ya a Isirayeli.

Tiyeni tiŵerenge 1 Samuyele 16:1 ndi 13

1-Ambuye anati kwa Samuyele, “ Kodi umulilira Sawulo mpaka liti, chimukanileni Ine iyeyo ngati mfumu ya a x? Udzadze nyanga yako ndi mafuta ndipo unyamuke; Ndikukutumiza iwe kwa Jesse wa ku Betelehemu. Ndasankha m’modzi mwa ana ache kuti akhale mfumu.”
13-Chomcho Samuyele anatenga nyanga ya mafuta ndipo anamudzodza Davide pa maso pa abale ache, ndipo kuchokera pa tsiku limenelo, Mzimu wa Ambuye unafika pa Davide mwa mphamvu.

-Sawulo atamwalira, a Isirayeli onse anapita kwa Davide kuti akamudzodze ufumu.

Tiyeni tiŵerenge 2 Samuyele 5:1-4

1-Mitundu yonse ya a x inapita kwa Davide ku Heburoni ndipo inati, “Ife ndi mnofu ndi magazi ako.
2-M’mbuyomo pamene Sawulo anali mfumu yathu, iwe unali m’modzi mwa anthu amene ankaŵatsogolera a x ku nkhondo. Ndipo Ambuye anati kwa iwe, “Udzaŵadyetsa anthu anga a x ndiponso udzakhala mtsogoleri wawo.
3-Pamene akulu akulu onse a a x anafika kwa mfumu Davide ku Heburoni, mfumu inakhazikitsa pangano ndi iwowo pa maso pa Ambuye, ndipo anamudzodza Davide kukhala mfumu ya a x.
4-Davide anali ndi zaka  30 pamene ankaloŵa ufu-



26-Davide, mwana wa Jesse anali mfumu wa dziko lonse la x.
27-Iye analilamulira dziko la x kwa zaka 40. Analamulira ku Heburoni kwa zaka 7, ndipo ku Yelusalemu, kwa zaka 33.
28-Ndipo anamwalira ali okalamba kwambiri, atasangalala ndi moyo wache wawutali ndi chuma ndiponso ulemelero. Solomoni, mwana wache ndi amene analoŵa ufumu m’malo mwa iyeyo.

-Solomoni atakhala mfumu ya a Isirayeli, kodi anachita chiyani?

Tiyeni tiŵerenge 2 Mbiri 2:1a

1-Solomoni analamulira zomaga nyumba ya Dzina la Ambuye.

-Solomoni anamanga nyumba ya Mulungu ngati m’mene bambo ache anamuwuzira.

-Dzina la nyumba imene Solomoni anamanga inkatchedwa kuti Nyumba ya Mulungu (Kachisi).

-Solomoni anamanga Nyumba ya Mulunguyi mu mzinda wa Yelusalemu.

-Mzinda wa Yelusalemu unali mzinda wawukulu kwambiri mu dziko la Kanani m’mene a Isirayeli ambiri ankakhalamo.

-Linga la miyala lalikulu kwambiri linazungulira mzinda wa Yelusalemu powuteteza mzindawo kwa adani a a Isirayeli.

-Nyumba ya Mulungu imene Solomoni anamumangira Mulungu, inkafanana ndi sakasa limene a Isirayeli ana-

-Mulungu adzatumiza Mpulumutsi amene adzakhale Mfumu mpaka kalekale.

-Kodi Mulungu anayiwala lonjezo lake lotumiza Mpulumutsi?
-Iyayi.

-Nthaŵi zonse Mulungu ankakumbukira za lonjezo Lache lotumiza Mpulumutsi wakuti adzatipulumutse ife ku tchimo, imfa ndi Satana.

-Davide asanamwalire, anakhonzekera zomanga nyumba ya Mulungu.

-Kenako, Davide anapereka tchito yomanga nyumba ya Mulungu ija kwa mwana wache wamamuna , Solomoni.

Tiyeni tiŵerenge 1 Mbiri 22:5-6

5-Daudi anati, "Mwana wanga Solomoni sanakule ndipo palibe chimene akuchidziŵa, koma nyumba ya Ambuye ikuyenera kumangidwa mosamalira kwambiri, molimbika ndipo yosangalatsa pa maso pa anthu a mitundu yonse. Chomcho ndikhaliratu okonzeka. Kenako Davide anayambiratu kusonkhanitsa zida zomangira nyumbayo asanamwalire.
6-Kenako anamuyitana Solomoni, mwana wache ndipo anamulamura kuti amange nyumba ya Ambuye, Mulungu wa a x.

-Kenako, Davide anamwalira, ndipo mwana wache, Solomoni anakhala mfumu ya a Isirayeli.

Tiyeni tiŵerenge 1 Mbiri 29:26-28



mu, ndipo analamulira kwa zaka 40.

-Sawulo ndi Davide sanali ofanana.

-Sawulo sankakhulupilira kuti iye anabadwira mu tchimo ndipo ali osiyana ndi Mulungu.

-Davide ankadziŵa kuti iye anabadwira mu tchimo ndipo ali osiyana ndi Mulungu.

-Sawulo sankakhulupilira kuti Mulugu amapereka chilango cha imfa pa tchimo lina lililonse.

-Davide ankadziŵa kuti Mulungu amapereka chilango cha imfa pa tchimo lina lililonse.

-Sawulo sankakhulupilira kuti Mulungu yekha ndi amene anakatha kumupulumutsa iye.

-Davide ankadziŵa kuti Mulungu yekha ndi amene anakatha kumupulumutsa iye.

-Sawulo sankakhulupilira mu chipangano cha Mulungu chakuti adzatumiza Mpulumutsi.

-Davide ankakhulupilira mu chipangano cha Mulungu chakuti adzatumiza Mpulumutsi.
Kudzamupulumutsa iye kwa Satana ndi imfa.

-Chifukwa chakuti Davide ankakhulupilira mwa Mulungu, analemba nyimbo zambiri zoŵapembedzera Ambuye.

-Davide analemba nyimbo zambiri zoŵapembedzera Ambuye zimene ziri M'buku la Mulungu, Bayibulo.

-Chifukwa chakuti Davide anali Mfumu ya a Isirayeli, iye

anali ndi ndalama zambiri.

-Chifukwa chakuti Davide anali mfumu ya a Isirayeli, iye anamanga nyumba yayikuru ya mitengo, miyala, golide ndi siliva.

-Tsiku lina Davide anayamba kuganiza za nyumba yache ndi kachisi wa Mulungu.

Tiyeni tiŵerenge 2 Samuyele 7:1-3

1-Mfumu itakhazikika m'nyumba yache ya ufumu ndipo Ambuye atamupumitsa kwa adani ache omuzunguli-ra,

2-anati kwa Natani Mneneri, "Ine ndili pano kukhala m'nyumba ya ufumu ya mtengo wapatali, pamene likasa lili mu lisasa.

3-Natani anayankha kwa mfumu kuti, "Chilichonse chimene ukuganiza m'maganizo ako, upitilire ndipo upan-ge chomwecho, pakuti Ambuye ali ndi iwe."

-Kodi Davide atatha kumanga nyumba yache, ankafuna kupanga chiyani?

-Davide ankafuna kuti amange nyumba ya Ambuye.

-Kodi Ambuye amafuna nyumba yakuti adzikhalamo?

-Mulungu amakhala ndipo ali palipose pa nthaŵi imodzi, ndipo samafuna nyumba yakuti adzikhalamo.

-Ngakhale kuti Mulungu samafuna nyumba yakuti adzikhalamo, Mulungu anasangalala chifukwa chakuti Da-vide amkaganizira za Iye.

-Kodi kenako Mulungu ananena chiyani kwa Davide?



Tiyeni tiŵerenge 2 Samuyele 7:12-13a

12-Ambuye anati, "masiku ako akadzakwana, ndipo iwe ukadzamwalira, Ine ndidzazikweza zidzukulu zako kuti zidzaloŵe m'malo mwako, zimenezi zidzachokera m'thupi lako, ndipo Ine ndidzawukhazikitsa ufumu wache.

13. Iyeyo ndi amene adzalimangire nyumba dzina langa."

-Ngakhale kuti Mulungu anasangalala ndi zakuti Davide ankaganiza za Iye, Mulungu ananena kuti Davide sadzamanga nyumba ya Mulungu.

-Kodi amene adzamange nyumba ya Mulunguyo adzakha-la ndani?
-Mwana wa mamuna wa Davide.

-Chifukwa chakuti Davide ankakhulupilira mwa Mulungu, Mulungu anapereka lonjezo kwa Davide.

-Apa pali zimene Mulungu analonjeza kwa Davide:

Tiyeni tiŵerenge 2 Samuyele 7:16

16-Ambuye anati kwa Davide, "Nyumba yako ndi ufumu wako zidzakhazikika mpaka kalekale pa maso pan-ga."

-Kodi lonjezo lalikuru limene Mulungu anapereka kwa Da-vide linali lotani?
-Mulungu analonjeza zakuti adzatumiza Mpulumutsi kupiti-ra mu zidzukulu za Davide.

-Lonjezo limeneli linali lofanana ndi lonjezo limene Mulun-gu anapereka kwa Abulahamu, Isaki ndi Yakobo.